# ASSEMBLY FOR ALL NATIONS

UTUMIKI WA AMAYI

**LILONGWE, MALAWI**

NOVEMBER 2023

## TABLE OF CONTENTS

1. Mawu Oyamba
2. Dzina
3. Cholinga
4. Zofunika kufikilidwa
5. Kugwira ntchito mu magulu
6. Utsogoleri wa utumiki wa amayi
7. Kukonza ndondomeko
8. Kayendetsedwe ka gulu la amayi mu maiko (National)
9. Kayendetsedwe ka gulu la amayi mu chigawo (Division)
10. Kayendetsedwe ka gulu la amayi mu boma (District)
11. Kayendetsedwe ka gulu la amayi mu dera (Cluster)
12. Malamulo oyendetsera bungwe la amayi pa mpingo
13. Mphamvu ndi ulamuliro
14. Kusiya ndi kuchotsedwa pa udindo
15. Zofunika pa udindo
16. Ma udindo mu bungwe la azimayi
17. Malamulo a unifolomu
18. Zowonjezela Zoyamba
19. Zowonjezela Zachiwiri

**MAWU OYAMBA**

Mpingo wa Assembly for All Nations (AfAN) uli ndi ma utumiki ambiri. Umodzi mwa ma utumikiwa ndi Utumiki Wa Amayi omwe umathandiza mpingo pa ntchito yolalikira uthenga wabwino ndiponso polambira Mulungu.

**1.0 DZINA**

Dzina lokhazikitsidwa ndi lovomelezedwa la utumiki wa amayi ndilo “**AMAYI A CHISOMO”** pansi pa mpingo wa Assembly for All Nations.

1. Mawu akuti utumiki wa amayi adzagwilitsidwa ntchito pa gulu lililonse la amayi pa mpingo iliwonse opezeka m’madera onse mu Assembly for All Nations
2. Malemba a m’Baibulo omwe utumiki wa amayi wayimapo ndi Mlaliki 9:10 “Chilichonse dzanja lako lapeza kuti lichite, chitani ndi mphamvu zanu zinse.
3. Mutu wathu ndiwo, “**TIMATUMIKILA CHIFUKWA CHA KHRISTU YESU**”.
4. Pemphero lathu likuchokera mu malemba a Baibulo amene ndi Masalimo 19:14 “Mulore mau a mkamwa mwanga ndi malingaliro a mu mtima mwanga akhale osangalatsa pa maso panu, Ambuye, thanthwe langa ndi m’womboli wanga.”
5. Utumiki wa amayi ungathe kutchedwanso “**Amayi a Chisomo**”.

**2.0 CHOLINGA**

Cholinga cha utumikiwu ndicho kuyambitsa, kukonza ndondomeko, kulumikiza, ndi kukweza ntchito za amayi mu mpingo wa Assembly for All Nations. Ntchito izi zidzathandiza kukweza moyo onse wa mphumphu wa mpingo ndi kuchita zinthu zothandiza kufukira osowa ndi otayika. Cholinga chake ndicho chiyanjano ndi ntchito yotumikira Khristu. Ntchito zonse zidzatsatila malamulo ndi chiphunzitso cha Assembly for All Nations.

**3.0 ZOFUNIKA KUFIKILIDWA**

Zofunika kufikilidwa ndi utumiki wa amayi zidzakhala izi:-

1. Kufikira amayi mu magawo onse a moyo wawo kuli konse komwe mpingo wa AfAN udzafikira.
2. Kulalikira Uthenga Wabwino kwa anthu onse.
3. Kuthandizira mpingo kulimgikitsa moyo wa uzimu, kuthupi ndi mu chikhalidwe.
4. Kuthandiza abusa ndi mabanja awo mu uzimu, kuthupi ndi mu chikhalidwe.
5. Kuthandiza mabanja onse mu mpingo m’mbali ya uzimu, kuzosowa zathupi ndi mu chikhalidwe.
6. Kuthandiza sukul za Baibulo mu za uzimu, ku zosowa zathupi ndi mu chikhalidwe.
7. Kuthandiza atsogoleri onse a Assembly for All Nations ndiponso kuthandiza mpingo onse mu uzimu, ku zosowa za thupi ndi mu chikhalidwe.
8. Kuthandiza mayiko onse omwe mpingo udzapezekamo mu uzimu, mu zosowa za thupi komanso mu chikhalidwe.

**4.0 KUGWIRA NTCHITO MU MAGULU.**

Padzakhala magulu osiyanasiyana ogwira ntchito mu utumiki wa amayi amene adzakhale ndi atsogoleri awo. Magulu awa adzakhala motere:-

a. Gulu la Utumwi
b. Gulu lopembedzera
c. Gulu loyang’anira chitukuko (projects)
d. Gulu la alangizi
e. Gulu la ntchito zaluso

### 4.1 Utumwi

Ili ndi bungwe loyang'anira usodzi, kupanga ophunzira, kudzala mipingo, komanso kukhala ndi udindo oyang'anira abusa.

### 4.2 Opembedzera

Ili ndi bungwe lomwe udindo wake ndi kusonkhanitsa anthu kumapemphero ndi ntchito zina zokhudzana ndi kupanga ophunzira a Khristu.

### 4.3 Chitukuko

Udindo wao ndi kuyambitsa ndi kulumikizitsa ntchito zikuluzikulu za chitukuko mu magulu onse a utumiki wa amayi.

### 4.4 Alangizi

Ili ndi bungwe la padera la amayi lomwe lili ndi kumvetsetsa pa kakulidwe ka moyo wa mzimayi mu milingo yosiyanasiyana ndipo ali ndi luntha (luso) lopeleka malangizo kuti amayi athe kudutsa magawo onse a moyo wao ndi chipambano. Utumikiwu ndi mbali izi: kutha msinkhu kwa asungwana, msinkhu olowa m;banja ndi kukhala ndi udindo otukula atsikana mu utsogoleri. Alangizi onse adzakhala amayi angwiro, okhwima mu chikhristu, amenenso amatha kusiyanitsa pakati pa chilangizo chotsatira miyambo ya makolo ndi chilangizo cha chikhristu. Adzagwira ntchito pamodzi ndi atsogoleri a ku National, ku Division, ku District, ku Cluster ndi pa mpingo uliwonse komanso bungwe la achinyamata maka gawo la atsikana.

### 4.5 Ntchito Zaluso

Adzakhala ndi udindo kuphunzitsa ntchito zosiyanasiyana monga kuphika, kuluka ndi zina zotero.

## 5.0 UTSOGOLERI

- Atsogoleri akuluakulu pa utumiki wa azimayi mu *AfAN Global* adzakhala Global Women Director, Deputy Global Women Director, Global Women Secretary, Deputy Global Women Secretary, Global Women Treasurer, Deputy Global Women Treasurer, komanso Global Women Missions Director.
- Atsogoleri akuluakulu a utumiki wa amayi pa *National* adzakhala Director, Deputy Director, Mlembi, Msungichuma, Women Division Directors ndi alangizi ochokera ku National.
- Atsogoleri adzakhala amayi amene amadziwa ndi kumvetsetsa utumiki wa amayi ndipo ali okhudzika ndi utumikiwu.

### 5.1 Mphamvu za Atsogoleri A Global komanso National Women Committee

Oyang'anira Utumiki wa Amayi pa dziko lonse adzasankhidwa ndi Bungwe lalikuru pa dziko lonse la AfAN Global Board. Oyang'anira Utumiki wa Amayi mdziko liri lonse adzasankhidwa ndi bungwe lalikuru mdzikomo la AfAN National Executive Committee motsatana ndi malamulo a akulu a mpingo wa Assembly for All Nations.

**5.2 (a) Udindo Wa Atsogoleri A Global**

1. Adzakhala pansi pa Global Board of Church Ministries (Bungwe Loyang'anira ma utumiki mu mpingo pa dziko lonse)
2. Adzamanga mpingo wa Assembly for All Nations pakuphunzitsa ndi kulimbikitsa amayi mu magawo onse.
3. Adzathandiza ndi kuphunzitsa atsogoleri a utumiki wa amayi mu magawo a kukonza ndondomeko, kulemba malipoti ndi kulumikizana.
4. Adzatumikira mu bungwe lokonza malamulo oyendetsera utumiki wa amayi wa Assembly for All Nations ndipo adzadalira chiphunzitso ndi malamulo ake.
5. Ayenera kukhala nawo pa misonkhano yonse ya Global Women's Committee ndi misonkhano yonse ya amayi mdziko.

**(a) Udindo Wa Atsogoleri A National**

6. Adzakhala pansi pa National Board of Church Ministries (Bungwe Loyang'anira ma utumiki mu mpingo mdziko liri lonse)
7. Adzamanga mpingo wa Assembly for All Nations pakuphunzitsa ndi kulimbikitsa amayi mu magawo onse.
8. Adzathandiza ndi kuphunzitsa atsogoleri a utumiki wa amayi mu magawo a kukonza ndondomeko, kulemba malipoti ndi kulumikizana.
9. Adzatumikira mu bungwe lokonza malamulo oyendetsera utumiki wa amayi wa Assembly for All Nations ndipo adzadalira chiphunzitso ndi malamulo ake.
10. Ayenera kukhala nawo pa misonkhano yonse ya National Wommen's Committee ndi misonkhano yonse ya amayi mdziko.

**5.3 MAINA AMENE ATSOGOLERI AYENERA KUTCHULIDWA**

**5.3.1 Oyang'anira Utumiki wa Amayi ku Global (Global Women's Director)**

1. Adzakhala ndi udindo oyendetsa ntchito zonse zopatsidwa ndi AfAN Global Board.
2. Adzakonza ndondomeko zabwino mogwirizana ndi ena okhuzidwa ndi utumikiwu ndipo adzazipeleka kwa wachiwiri wa Global President wa Assembly for All Nations pa dziko lonse kuti azivomeleze.
3. Adzakhala ndi kuthekela konse kuti atukule ndi kupeleka ndondomeko zonse za ntchito yake ndi za chuma choyendetsa utumikiwu.
4. Adzayitanitsa misonkhano ndi kukonza zokambirana ku msonkhano mogwirizana ndi Mlembi.
5. Adzakhala nawo pa misonkhano yonse ya amayi pa dziko lonse mokhulupilika.
6. Adzakhala wapampando wa misonkhano yonse; koma ali nayo mphamvu yosankha munthu wakumuyimilira.

**5.3.2 Wachiwiri Oyang'anira (Deputy Global Women Director)**

1. Adzakhala wachiwiri kwa oyang'anira (Director).
2. Adzakhala mnkhala pampando wa ntchito zonse ndi mabungwe onse aang'ono okhazikitsidwa ndi utumiki wa amayi.
3. Ayenera kugwira ntchito zonse zopatsidwa ndi a Director.
4. Apezeke mokhulupilika ku misonkhano yonse yokonzedwa ndi utumiki wa amayi ku Global.

### 5.3.3 Mlembi Wamkulu (Global Women Secretary)

1. Adzasunga  mabuku onse ndi zonse zolembedwa mu misonkhano.
2. Adzagawa zonse zoyenera kudziwidwa ndi gulu la amayi.
3. Adzapezeka mokhulupilika mu misonkhano yonse ya Global.
4. Adzayenera kuthandizira a Director pamene asowa chithandizo pa ntchito yawo.

### 5.3.4 Wachiwiri kwa Mlembi Wamkulu (Deputy Global Women Secretary)

1. Adzakhala wachiwiri kwa mlembi.
2. Adzathandiza a Director pamene asowa thandizo.
3. Adzapezeka pa misonkhano ya Global mukhulupilika.

### 5.3.5 Msungichuma (Global Women Treasurer)

1. Adzasunga ndondomeko zonse zokhudza chuma.
2. Adzayenela kupezeka mokhulupilika mu misonkhano yonse ya Global.
3. Adzandiza a Director ntchawi zonse asowa thandizo.
4. Adzapeleka ndondomeko ya momwe ndalama za utumiki zikuyendera.

### 5.3.6 Wachiwiri kwa Msungichuma (Deputy Global Women Treasurer)

1. Adzakhala wachiwiri kwa msungichuma.
2. Adzagwira ntchito zonse zopatsidwa ndi a Director a utumiki wa amayi.
3. Adzapeleka mukhulupilika mu misonkhano yonse ya Global.
4. Adzakhala ndi udindo wopeza njira zopezera chuma.

### 5.3.7 Mlangizi Wamkulu

Mlangizi wamkulu wa utumiki wa amayi pa pa dziko lonse lapansi adzakhala mkazi wa Global President wa Assembly for All Nations. Mlangizi wamkulu wa utumiki wa amayi pa National adzakhala mkazi wa National Pastor wa Assembly for All Nations mu dziko liri lonse. Izi zidzchitika chimodzimodzi pa magawo ndi ma udindo onse mu ma Division, nkazi wa a Division Director; ku District; mkazi wa a District Director, mu Cluster; mkazi wa a Cluster Director, ndipo mu mpingo adzakhala mkazi wa Abusa pa mpingowo.

## 6.0 KUKONZA NDONDOMEKO

Mu bungwe lokonza ndondomeko ya ntchito mukhale anthu awa: atsogoleri a komiti ya Global ya Amayi, atsogoleri a gulu lopembedzela, atsogoleri a za chitukuko, atsogoleri a utumiki, alangizi ndi atsogoleri a gulu la ntchito zaluso. Adzakumana kuti akonze ndondomeko za nthawi yochepa (short term) ndi ndondomeko za nthawi yayitali (long term).

### 6.1 Misonkhano

Misonkhano yokonza ndondomeko idzachitika pafupipafupi kuti pakhale mpata olimbikitsa utumiki ndi chiyanjano.

### 6.2 Za Chuma

*a) Utumiki wa amayi udzagwiritsa ntchito njira izi zopezela ndalama:*

i. Chakhumi chochokera ku ma National Women Ministry.
ii. Tsiku la amayi lomwe linakhazikitsidwa kuchikera ku malamulo a akulu a Assembly for All Nations.
iii. Zochitika zopangidwa ndi magulu amene ali ndi chidwi (njira zosiyanasiyana zopezera chuma).
iv. Za chitukuko chopangidwa ndi utumiki wa amayi.

b) *Ndalama za utumiki wa amayi*
   i. Sizidzagwira ntchito popanda chilolezo cha atsogoleri a m'komiti.
   ii. Zidzasungidwa ku banki lovomerezeka ndi utumiki wa amayi.

### 6.3 Ntchito za Utumiki za Chitukuko

Ntchito zonse za chitukuko zidzakhala zogwilizana ndi mfundo za mpingo ndipo zidzalinganizidwa mofanana ndi madera onse a utumiki omwe alembedwa mu buku la utumiki wa amayi.

### 6.4 Utumiki Owonjezera (Auxillary)

Povomelezedwa ndi abusa ndi akulu a mpingo, utumiki wa amayi udzathandiza alangizi, utumiki owonjezerapo omwe cholinga chake ndi kulimbikitsa atsikana ku utsogoleri. Maphunziro adzapelekedwa kwa asungwana ndi chithandizo cha uzimu ndi zonse zofunikira pa utumiki owonjezera.

## 7.0 KASINTHIDWE KA BUKU ILI

Kusintha kulikonse mu buku ili kudzakhala kovomelezedwa ndi bungwe lalikulu loyendetsa mpingo wa Assembly for All Nations pa dziko lonse (AfAN Global Board).

## 8.0 KAYENDETSEDWE KA UTUMIKI WA AMAYI MU MAIKO (NATIONAL)

### 8.1 Komiti ya National

1. Padzakhala ma membala asanu ndi awiri (7) mu komiti yoyendetsa utumiki wa amayi mu dziko liri lonse (National), amene ali ndi mtsogoleri ndi wachiwiri wake, mlembi ndi wachiwiri wake ndi msungichuma ndi wachiwiri wake ndi woyang'anira utumwi. Ma membala a komiti imeneyi adzakhala ma Division Directors.
2. Atsogoleri adzatsatira malamulo a utumiki wa amayi mu Assembly for All Nations ndi kukweza chiphunzitso cha mpingo wathu.
3. Atsogoleri adzakhala pansi pa Director mu utumiki wa amayi ku National komanso pansi pa Deputy National Pastor.
4. Mtsogoleri wa amayi ku National akhoza kusankhidwa kukhala membala wa wa komiti ya amayi ku AfAN Global.

### 8.2 Ma udindo a Komiti ya National

1. Adzakhala oyankha kwa komiti yayikulu ya utumiki wa amayi ku AfAN Global Women.
2. Adzaphunzitsa atsogoleri ku Division, District, Cluster ndi pa mpingo.
3. Adzayambitsa ntchito za chitukuko ku National.
4. Adzathandiza misonkhano ya amayi ku AfAN Global.
5. Adzakonza ndi kukhazikitsa ofesi ya amayi ku National.
6. Adzapezeka mokhulupilika pa misonkhano ya AfAN Global Women.

### 8.3 Chuma cha utumiki wa amayi mu dziko liri lonse (National Women Ministry)

1. Ndalama za National zidzachokera ku chakhumi chochokera ku ma utumiki a amayi ku ma Division.
2. Mabungwe (komiti) a ku National.
3. Zopeleka zomwe zidzatengedwe ku misonkhano ya National.
4. Ndalama sizidzagwira ntchito popanda chilolezo cha ma membala a komiti maka mtsogoleri wamkulu.
5. Ndondomeko ya momwe zachuma ikuyendera idzapelekedwa ku msonkhano wa National.
6. Chakhumi cha ndalama zonse chidzapelekedwa ku komiti yayikulu ya utumiki wa amayi ku AfAN Global Women Ministry.
7. Ndalama zidzasungidwa ku banki lovomelezedwa ndi komiti ya amayi.
8. Iwo adzayambitsa ndi kupangitsa ntchito zopezera ndalama.

## 9.0 KAYENDETSEDWE KA UTUMIKI WA AMAYI KU MA DIVISION

### 9.1 Komiti ya Division

5. Pakhale ma membala asanu ndi awiri (7) mu komiti yoyendetsa utumiki wa amayi mu Division, amene ali ndi mtsogoleri ndi wachiwiri wake, mlembi ndi wachiwiri wake ndi msungichuma ndi wachiwiri wake ndi woyang'anira utumwi.
6. Atsogoleri adzatsatira malamulo a utumiki wa amayi mu Assembly for All Nations ndi kukweza chiphinzitso cha mpingo wathu.
7. Atsogoleri adzakhala pansi pa Director mu utumiki wa amayi ku National ndi kwa wamkulu wachiwiri wa Division (ku Division yawo).
8. Mtsogoleri wa amayi ku Division adzakhalanso membala wa komiti ya amayi ku National.

### 9.2 Ma udindo a Komiti ya Division

7. Adzakhala oyankha kwa komiti yayikulu ya utumiki wa amayi ku National.
8. Adzaphunzitsa atsogoleri ku District, Cluster ndi pa mpingo.
9. Adzayambitsa ntchito za chitukuko ku Division.
10. Adzathandiza misonkhano ya amayi ku National.
11. Adzakonza ndi kukhazikitsa ofesi ya amayi ku Division.
12. Adzapezeka mokhulupilika pa misonkhano ya Division.

### 9.3 Chuma cha Division

9. Ndalama za Division zidzachokera ku chakhumi chochokera ku ma utumiki a amayi ku ma district.
10. Mabungwe (komiti) a mu Division.
11. Zopeleka zidzatengedwe ku misonkhano ya Division.
12. Ndalama sizidzagwira ntchito popanda chilolezo cha ma membala a komiti maka mtsogoleri wamkulu.
13. Ndondomeko ya momwe zachuma ikuyendera idzapelekedwe ku msonkhano wa Division.
14. Chakhumi cha ndalama zonse chidzapelekedwa ku komiti yayikulu ya utumiki wa amayi ku National.
15. Ndalama zidzasungidwa ku banki lovomelezedwa ndi komiti ya amayi.
16. Iwo adzayambitsa ndi kupangitsa ntchito zopezera ndalama.

## 10.0 KAYENDETSEDWE KA UTUMIKI WA AMAYI KU DISTRICT

### 10.1 Komiti ya District

1. Komiti yoyendetsa utumiki wa amayi ku district idzakhala ndi mamembala asanu ndi awiri (7) ndipo adzakhala motere: mtsogoleri ndi wachiwiri wake, mlembi ndi wachiwiri wake, msungichuma ndi wachiwiri wake ndi woyendetsa utumwi.
2. Atsogoleri adzatsatira malamulo oyendetsera utumiki wa amayi mu Assembly for All Nations ndi kukweza chiphunzitso cha mpingo.
3. Adzakhala pansi pa komiti ya Division ndipo adzatsatira ndondomeko ndi ntchito zonse za utumiki wa amayi ku National.

### 10.2 Maudindo a Komiti ya District

1. Adzayambitsa ntchito yokhazikitsa utumiki w amayi mu mpingo ya m'madera awo onse.
2. Adzaphunzitsa amayi ku District za maziko ndi cholinga cha utumiki wa amayi ndi kulimbikitsa amayi ndi kuti ayambe ntchito za chitukuko.
3. Adzayendera mipingo kuti alimbikitse ndi kupeleka mhamvu ku magulu a amayi a mu mpingo.
4. Adzapezeka pa mis onkhano ya District ndi Division.
5. Adzakumana monga mwa ndondomeko yoyenera ku misonkhano ya District.

### 10.3 Chuma cha District

1. Ndalama zidzachokera ku chakhumi cha utumiki wa amayi ku ma Cluster onse mu district.
2. Adzayambittsa ntchito zapadera zopezera ndalama zothandizira zosowa za mu District.
3. Ndalama sizidzagwiritsidwa ntchito popanda chilolezo cha komiti.
4. Ndalama zonse zidzasungidwa ku banki yovomelezeka.
5. Adzapeleka chakhumi chandalama zonse ku komiti ya utumiki wa amayi ya Division.
6. Adzayambitsa ndi kulimbikitsa ntchito zopezela chuma.

## 11.0 MALAMULO OYENDETSELA UTUMIKI WA AMAYI MU CLUSTER

### 11.1 Komiti ya Amayi mu Cluster

1. Komiti idzakhala ndi anthu asanu ndi awiri (7) omwe adzakhale motere: mtsogoleri ndi wachiwiri wake, mlembi ndi wachiwiri wake, msungichuma ndi wachiwiri wake ndi wiyendetsa ntchito za utumwi
2. Atsogleriwa azasankhidwa ndi komiti yayikulu ya abusa mu Cluster.
3. Adzayenera kutumikira kwa zaka ziwiri (2).
4. Adzathandiza mpingo wa pa malo ndi kutsatira malamulo onse a Assembly for All Nations.
5. Adzakhaala pansi pa komiti ya amayi mu District.

### 11.2 Maudindo a Atsogoleri mu Cluster

1. Adzathandiza kukhazikitsa utumiki wa amayi pa mipingo ya Assembly for All Nations.
2. Adzayenera kupezeka nawo pa misonkhano ya mu Cluster, District, Division ndi National.

3. Ntchito zonse za mu Cluster zodzakhala pansi pa ulamuliro wa ma komiti akulu a utumiki wa amayi.
4. Adzathandiza ntchito zonse za utumiki wa amayi.

### 11.3 Chuma cha mu Cluster

1. Chakhumi ndi ndalama zonse zolandilidwa kuchokera ku mipingo yonse ya mu Cluster ndi zopeleka zonse zapadera zidzapita ku komiti ya amayi ya District.
2. Atsogoleri a mu Cluster adzalandira zopeleka za misonkhano yonse ya komiti ya mu cluster.
3. Ndalama zonse zidzasungidwa ku banki yovomelezeka.
4. Ndalama za Cluster siziloledwa kubwereketsedwa ndi atsogoleri kapena wina aliyense.
5. Ndondomeko ya momwe ndalama zikuyendera upelekedwe ku msonkhano uliwonse wa cluster.
6. Adzatenga nawo gawo pa ntchito zonse zopezera chuma.

## 12.0 MALAMULO OYENDETSELA UTUMIKI WA AMAYI PA MPINGO

### 12.1 Dzina

Dzina lathu lidzakhala “**Utumiki wa Amayi**” lodziwika kuti “**Amayi a Chisomo**”.

### 12.2 Umembala (Zoyeneleza)

Amayi a Chisomo akhale obadwanso mwatsopano, mamembala a mpingo omwe ali ndi anthu a mbiri yabwino pa mpingo pawo. Iwo akhale okwanilitsa malamulo onse owayeneleza kukhala membala pa mpingo alembedwa mu malamulo a akulu a Assembly for All Nations.

### 12.3 Utsogoleri (Atsogoleri)

1. Akhale amayi opulumutsidwa ndi amene ali ndi mbiri yabwino pa mpingo pawo.
2. Akhale pansi pa ulamuliro wa m’busa wa pa mpingo ndi pansi pa komiti yayikulu ya amayi kuyambira ku National mpakana pa Cluster.
3. Atsatire chiphunzitso chonse cha Assembly for All Nations.
4. Akhale ma membala okhulupilika amene awonetsera kukhulupilika kwawo pa ntahwi yayitali.
5. Akhale ndi mbiri yabwino ndi opewa mikangano.
6. Adzasankhidwa ndi abusa kuti atumikire kwa chaka chimodzi kapena zaka ziwiri. Komiti isankhidwe ndi Mayi Busa mogwirizana ndi mtsogoleri wa utumiki wa amayi pa mpingo.
7. Adzachotsedwa ngati sakukwaniritsa mulingo wa Assembly for All Nations mu ntchito ndi moyo wa pagulu ndi moyo wa paokha.
8. Akhale ndi udindo umodzi okha basi (pokhapokha ngati pali zifukwa zina zokwanira) kuti awonetsetse kuti utumiki wa amayi ukuyenda bwino.

### 12.4 Zochitika

1. Adzathandiza mpingo m’madera onse ofunikira.
2. Adzathandizira Abusa ndi banja lawo mu uzimu, mchikhalidwe, komanso mu zosowa zathupi.
3. Adzathandiza ntchito zonse za utumiki wa amayi.
4. Adzathandiza ku sukulu ya Bayibulo ndi utsogoleri wa Assembly for All Nations.

### 12.5 Maudindo a Komiti ya Utumiki wa Amayi pa Mpingo

1. Adzayenela kupezeka mokhulupilika ku misonkhano yonse ya Cluster, District, Division ndi National.
2. Adzakhala pansi pa utsogoleri wa m'busa komanso mayi busa.
3. Adzathandiza ntchito zonse za utumiki wa amayi.

### 12.6 Mkhalapampando (Chairperson)

1. Adzakhala membala wamkulu ku komiti ya utumiki wa amayi mu Cluster.
2. Adzatsogolera utumiki onse wa Amayi pa mpingo m'misonkhano.
3. Adzatsogolera ntchito zonse za tsiku ndi tsiku za utumiki wa amayi pa mpingo.
4. Mogwirizana ndi Mayi Busa, adzasankha anthu kuti agwire ntchito zosiyanasiyana mu utumiki wake.
5. Adzatsogolera misonkhano ya komiti.
6. Adzapeleka chakhumi pa mpingo wake.

### 12.7 Mlembi

1. Adzasunga ndi kulemba zokambirana zonse.
2. Adzathandiza utumiki wonse moyenera komanso zochitika zina zonse.
3. Adzathandiza mnkhalapampando moyenera.
4. Adzapezeka mokhulupilika ku misonkhano yonse ya utumiki wa amayi.
5. Adzapeleka chakhumi ku mpingo wake.

### 12.8 Msungichuma

1. Adzasunga ndondomeko yonse ya chuma cholandilidwa ndi kugwiritsidwa ntchito, ndipo adzasunga buku la dongosolo la ndalama.
2. Adzathandiza mnkhalapampando moyenerera.
3. Adzapezeka pa misonkhano ya utumiki wa amayi mokhulupilika.
4. Adzsunga ndalama mosamalitsa ku banki yovomelezeka.
5. Saloledwa kubwereka ndalama za utumiki kapena kubweleketsa kwa ena.
6. Adzapeleka dongosolo la momwe chuma chikuyendera kwa mwezi uliwonse.
7. Adzapeleka chakhumi ku mpingo wake.

### 12.9 Zachuma

1. Amayi adzapeleka zopeleka nthawi zonse akasonkhana.
2. Amayi adzagwira ntchito yopadera yopezera chuma.
3. Ndalama zidzagwira ntchito yotumikira zosowa zosiyanasiyana mwakugwirizana.
4. Adzathandiza ntchito za Cluster, District, Division monga kuyenera kutero.
5. Chakhumi cha utumiki wa amayi pa mpingo uliwonse chiperekdwe ku thumba la Cluster.

### 12.10 Misonkhano

1. Utumiki wa Amayi pa mpingo uliwonse ukhale ndi kukumana kwapafupipafupi kuti alambire, aphunzire mau a Mulungu, kupemphera ndi kukhala ndi chiyanjano.
2. Adzisankhire masiku amene sadzasokoneza ntchito ndi misonkhano ina ya pa mpingo.
3. Ngati membala waphwanya malamulo, ayenera kuchenjezedwa, ngati sasintha ayenera kuyimikidwa.

4. Ngati mtsogoleri kapena membala achita tchimo la chigololo kapena kuba, ayenera kuchotsedwa mu kaundula wa ma membala mwamsangamsanga.
5. Ngati membala salemekeza utsogoleri, ayambitsa mikangano, sakumvera abusa, ayenera kuchotsedwa.
6. Ngati membala anayimikidwa ku mpingo, sayenera kukhala membala mw utumiki wa amayi.

## 13.0 MPHAMVU NDI ULAMULIRO

1. Atsogoleri onse a utumiki wa amayi adzakhala pansi pa ulamuliro wa komiti yayikulu ya utumiki wa amayi ma dziko lonse la pansi (Global), National, Division, District, komanso Cluster.
2. Adzapeleka malipoti kwa oyang'anira utumikiwu.
3. Komiti idzakhala ndi mphamvu yopeza kapena kukongola ndalama zogwiritsa ntchito mu utumiki ndi chikole chomwe iwo adzasankha.
4. Makomiti a pamwamba adzakhala ndi mphamvu yochotsa kapena kuyimika mamembala a makomiti amene ali pansi pawo.

## 14.0 KUSIYA NDI KUCHOTSEDWA UDINDO

### 14.1 Kusiya udindo kwa mtsogoleri.

Mtsogoleri aliyense adzaloledwa kusiya utsogoleri ngati adzakhala ndi makalata a umboni atatu ochokera kwa a chipatala ovomelezeka, osonyeza kuti mtsogoleri sakupeza bwino mu maganizo ndi mthupi.

### 14.2 Kuchotsedwa kwa mtsogoleri

Mtsogoleri aliyense adzachotsedwa ngati:

a. Adzasemphanitsa/adzalakwitsa pa malamulo, mfundo ndi ziganizo za chiphunzitso cha mpingo wa Assembly for All Nations.
b. Alephera kugwira ntchito ndi kulephera kupereka ndondomeko zabwino, ndondomeko zogwilira ntchito, ndi malipoti ofunikira.
c. Alephera kupezeka pa misonkhano itatu yotsogozana popanda zifukwa zokwanira.

## 15.0 ZOFUNIKA PA UDINDO

1. Atsogoleri a pa mpingo adzakhala otumikira kwa chaka chimodzi kapena zaka ziwiri ndipo angathe kusankhidwanso.
2. Makomiti onse a dela (cluster), District, Division, National komanso Global adzatumikira kwa zaka ziwiri ndipo angathe kusankhidwanso.

## 16.0 MAUDINDO MU UTUMIKI WA AZIMAYI

Assembly for All Nations **Global Board**

Komiti ya utumiki ya **AfAN Global Women**

Komiti ya utumiki wa Amai pa **National**

Komiti ya utumiki wa Amai pa **Division**

Komiti ya utumiki wa Amai pa **District**

Komiti ya utumiki wa Amai pa **Cluster**

Komiti ya utumiki wa Amai **pa Mpingo**

## 17.0 MALAMULO A YUNIFOLOMU

### 17.1 Kufunika kwa Yunifolomu ya Utumuki wa Amayi

Ubwino wa unifolomu ya utumiki wa amayi ndi:

17.1.1 Kuonetsa umodzi wa amayi.

17.1.2 Kuonetsera umodzi mu chikhalidwe, malingaliro komanso m'chiphunzitso.

17.1.3 Kuonetsera kuti amayi ali ndi cholinga chimodzi.

17.1.4 Kuonetsa kuti amayi mu Assembly for All Nations ali ndi chizindikiro chimodzi.

17.1.5 Kuonetsa kuti amayi amasangalala ndipo akukweza mpingo wa Assembly for All Nations.

### 17.2 Malamulo a Mwambo Obvekedwera Yunifolomu

17.2.1 Adzatsogolera mwambowu ndi abusa pa mpingo omgwirizana ndi atogoleri a utumiki wa amayi a pa mpingopo ndi a dela (Cluster).

17.2.2 Udzachitika pagulu pamene onse obvekedwa atakwanilitsa zones za m'gawo 16.3 la malamulowa.

17.2.3 Pamwambowu padzakhala zochitika za chisangalaro.

### 17.3 Zoyeneleza Obvekedwa Yunifolomu oa Utumiki wa Amayi.

17.3.1 Yunifolomu ndiyololedwa kwa amayi okhawo amene ali mamembala a Assembly for All Nations. Muone gawo 17.0 la malamulowa kuti mudziwe munthu amene angathe kukhala membala ovomelezeka.

17.3.2 Mamembala adzayenera kutsata mokhulupilika ziphunzitso zones za Assembly for All Nations. Izi zidzayenerakutsatidwa mokhulupilika: kupereka chakhumi, kusonkhana ku mpingo, kupezeka pa misonkhano ya utumiki wa amayi ndi zina.

17.3.3 Amayi ovomelezedwa ayenera kuchita maphunziro a masiku awiri (2) a malamulo ovalira yunifolomu ndi kuphatikizapo buku la malamulo a utumiki wa amayi.

### 17.4 Malamulo ndi zoyenera kutsata za Yunifolomu.

17.4.1 Yunifolomu ivalidwe pa misonkhano yokhayo yovomelezeka ndi mpingo komanso misonkhano ina yapadera monga misonkhano yaikulu, misonkhano ikulu-ikulu ya utumiki wa amayi pa mpingo, pa maliro ndi Madera ena ovomelezedwa.

17.4.2 Yunifolomu idzavalidwanso pa zina zochitika zomwe sizinalembedwe pa malamulo a utumiki wa amayi ngati mamembala a utumikiwu abvomelezana kutero.

17.4.3 Yunifolomu idzavomelezedwa kwa mamembala oyenera pa mwambo wa kveka ndi kukhazikitsa yunifolomu.

17.4.4 Membala amene wamaliza maphunziro ayenera kukhala ndi zinthu izi: Baibulo lakelake, buku la Nyimbo za Chitsitsimutso, ndi buku la malamulo a utumiki wa amayi. Izi zidzawonetsedwa pa nthawi yakuvekedwa ndi kukhazikitsa yunifolomu.

17.4.5 M'busa ndi nkazi kapena mwamuna wake pamodzi ndi atsogoleri a utumiki wa amayi ali ndi ulamuliro ochita mwambo oveka ndi kukhazikitsa amai mu yunifolomu.

17.4.6 Yunifolomu idzakhalebe ya Assembly for All Nations nthawi zonse osati ya amayi paokha ngakhale kuti anagula ndi ndalama zawo.

### 17.5 Mtundu wa Yunifolomu, Kusamala ndi Mavalidwe ake.

17.5.1 Yunifolomu idzakhala ndi patani ya masokedwe amodzi mu dziko liri lonse monga momwe bungwe lalikuru la Assembly fo All Nations m'dzikomo (NEC) lagwirizanilana.

17.5.2 Mtundu wake ndi siketi ya golide (deep gold), Malaya a kumtunda (bulawuzi) oyera (white), duku loyera komanso msapato wakuda.

17.5.3 Mtundu oyera ma Malaya a kutunda (Blouse) ukuyankhula za chiyero ndi chilungamo cha Yesu Khristu.

17.5.4 Mtundu wa golide ukuyankhula za mzinda wa golide omwe Mulungu wathu anatikonzera omwe tikakhalako ndi iye tikachoka pa dziko lino lapansi. **(Chibvumbulutso21:21)**

17.5.5 Yunifolomu ingathe kuvalidwa popanda msapato yakuda kwa amene alibe msapato.

17.5.6 Yunifolomu isamalidwe bwino nthawi zones. Langizo ndilakuti yunifolomu isavalidwe wamba panthawi yomwe munthu wafuna payenkha kapenanso mkati mwa chitenje.

17.5.7 Amayi alangizidwe kuti yunifolomu isavalidwe paliponse. Cholinga cha langizoli ndi kuti yunifolomu isamalike ndi kuti isathe mwachangu kapena kusintha maonekedwe.

## 18.0 ZOWONJEZERA ZOYAMBA

**Zoyeneleza kukhala Membala**

(Gawo ili linatengedwa kuchokera mu buku lalikuru la mayendedwe a Assembly for All Nations pa Mutu otchedwa "Membala" pa malamulo oyendera mpingo.)

Munthu angathe kulandilidwa pa mpingo akakwanilitsa zofunikira izi (zomwezo zimayeneleza munthu kuti ayambe nawo utumiki wa amayi):

1. Akhale obadwa mwatsopano (Yohane 3:3-8)
2. Akhale moyo wa chiyero (1 Petro 1:15)
3. Akhale obatizidwa mmadzi (Machitidwe 2:38)
4. Akhale okhulupilika mu chakhumi mu zones zomwe amapeza ndi zopeleka ku mpingo (Malaki 3:10)
5. Akhale okhulupilika mu chiphunzitso cha Assembly for All Nations.

*Onse ofuna kukhala mamembala aunikidwe ndi m'busa ndi akulu a mpingo, ndipo alandilidwe pa msonkhano wagulu la onse mu nthawi yolanbila komanso maina awo alembedwe mu buku la kaundula wa mamembala a pa mpingo.*

## 19.0 MALIRO

Pa mwambo wa maliro padzawelengedwa ma verse ochokera pa Masalimo 121 vs. 1 – 8.

## 20.0 ZOWONJEZERA ZACHIWIRI

***ZIPHUNZITSO ZA CHIKHULUPILIRO CHATHU***

Ife amayi a Assembly for All Nations timakhulupilira:

### A. Malembo Owuziridwa

Malembo amene ndi chipangano cha kale komanso chatsopano ndi owuziridwa ndi Mulungu ndipo ndi vumbulutso la Mulungu kwa munthu, muyeso wosalakwa ndi wa ulamuliro wa chikhulupiliro m'makhalidwe (2 Timoteo 3:15-17)

### B. Mulungu M'modzi Woona.

Mulungu m'modzi woona anadzivumbulutsa yekha monga wamoyo wachikhalire "INE NDINE", Mlengi wa kumwamba ndi dzko lapansi ndi mombolo wa anthu. Ndipo wapitilira kudzivumbulutsa yekha ngati Atate, Mwana ndi Mzimu Woyera (Deuteronomo 6:4; Yesaya 43:10; Mateyu 28:19; Luka 3:22).

### C. Umulungu wa ambuye Yesu Khristu

Ambuye Yesu Khristu ndi Mwana wa Mulungu wachikhalire. Malembo amanena motsimikiza za:

1. Kubadwa kwake mwa namwali (Mateyu 1:23; Luka 1:31, 35).
2. Moyo wake wopanda tchimo (Ahebri 7:26; 1 Petro 2:22).
3. Zozizwa zake (Machitidwe 2:22; 10:38).
4. Ntchito Yake yotilowera m'malo mwathu pa mtanda (1 Akorinto 15:3; 2 Akorinto 5:21)
5. Kuuka kwake kwa akufa ndi thupi lake (Mateyu 28:6; LLuka 24:39; 1 Akorinto 15:4)
6. Kukwezedwa kwake kudzanja la Mulungu (Machitidwe 1:9-11; 2:33; Afilipi 2:9-11; Ahebri 1-3).

### D. Kugwa kwa Munthu

Munthu analengedwa wabwino ndi wolungama; pakuti Mulungu anati, "Tipange munthu mu chifanizo chathu, monga mwa chikhalidwe chathu." Koma munthu posankha kuchimwa anagwa nabweletsa infa ya m'thupi ngakhalenso ya mu uzimu, imene ndi kulekanitsidwa ndi Mulungu (Genesis 1:26, 27; 2:17; 3:6; Aroma 5:12-19).

### E. Chipulumutso cha Munthu

Chiyembekezo chokhacho cha munthu kuti awomboledwe ndi kupyolera mwa mwazi wokhetsedwa ndi Yesu Khristu Mwana wa Mulungu.

a. **Zofunikira pa Chipulumutso**

   Chipulumutso chimalandiridwa mwa kutembenukira kwa Mulungu ndi kukhulupilira Ambuye Yesu Khristu. Mwa kutsukidwa mu kubadwanso ndi makonzedwe a Mzimu Woyera, woyesedwa wolungama ndi chisomo mwa chikhulupiliro, munthu amasanduka wolowa wa Mulungu kolingana ndi chiyembekezo cha moyo wosatha. (Luka 24:27; Yohane 3: 1-5, 16; Aroma 10:13-15; Aefeso 2:8; Tito 2:11; 3:5-7)

**b. Chitsimikizo cha Chipulumutso**

Chitsimikizo cha mkati cha chipulumutso ndi umboni wa Mzimu (Aroma 8:16), Chitsimikizo cha kunja kwa anthu onse ndi moyo wa chilungamo ndi chiyero chenicheni (Aefeso 4:24; Tito 2:12)

## F. Zoikika za Mpingo

**a. Ubatizo wa M'madzi**

Choikika cha ubatizo wakumiza m'madzi ndi cholamulidwa m'Malembo. Onse amene atembenuka mtima nakhulupilira Khristu kukhala Mpulumutsi ndi Mbuye wao ayenera kubatizidwa m'madzi. Potero amasonyeza kwa aliyense kuti anafa ndi Khristu ndi kuti anaukitsidwa nayenso pamodzi m'moyo watsopano. (Matetu 28:19; Maliko 16:16; Machitidwe 10:47; Aroma 6:4)

**b. Mgonero wa Ambuye**

Mkate pamodzi ndi vinyo wochoka ku chipatso cha mpesa ndi chithunzithunzi cha m'ene ife timagawana naye Ambye wathu Yesu Khristu Umulungu wake (2 Petro 1:4); chikumbutso cha mazunzo ake ndi imfa yake (1 Akorinto 11:26) ndipo ulamuliro kwa okhulupilira onse "kufikira akadza iye."

## G. Ubatizo wa Mzimu Woyera

Okhulupilira onse ndi oyembekezeka ndipo ayenera kunitsotsa ndi khama lonse lonjezo la Atate, ubatizo wa Mzimu Woyera ndi moto kolingana nsi lamulo la Ambuye wathu Yesu Khristu. Ichi ndi chimene anthu onse anali kulandira mu mpingo wa chikristu woyambilira uja. Uvekedwa ndi mphamvu pa moyo ndi utumiki, kuperekdwa kwa mphatso ndi ntchito zake mu ntchito ya utumiki ndi zinthu zimene zimadza ndi ubatizowu (Luka 24:49; Machitidwe 1:4-8; 1 Akorinto 12:31). Ubatizowu usiyana ndi kubadwanso mwatsopano, ndipo umachitika pambuyo pa kubadwa mwatsopano (Machitidwe 8:12-17; 10:44-46; 15:5-9). Ndi ubatizowu wa Mzimu Woyera, pamakhala kusefukira kwa chidzalo cha mzimu (Yohane 7:37-39; Machitidwe 2:43; Ahebri 12:28), kudzipatulira kwathunthu kwa Mulungu ndi kudzipeleka ku ntchito Yake (Machitidwe 2:42), ndi chikondi chochita choposa kale cha pa Khristu, pa mau Ake ndi otayika (Maliko 16:20).

## H. Chizindikiro cha Ubatizo

Ubatizo wa okhulupilira mwa Mzimu Woyera umadziwika ndi chizindikiro choyamba cha kulankhula ndi malilime ena monga Mzimu wa Mulungu alankhulitsira (Machitidwe 2:4). Kulankhula ndi malilime kumeneku ndikofanana mukhalidwe lake lenileni ndi mphatso ya malilime (1 Akorinto 12:4-10, 28), koma kosiyana ponena za cholinga ndi kugwiritsa ntchito kwake.

## I. Chyeretso

Chiyeretso ndi machitidwe a kudzipatula ku chinthu choipa ndi kudzipeleka kwa Mulungu (Aroma 12:1, 2; Atesalonika 5:23; Aheberi 13:12). Malembo atiphunzitsa za moyo wa "chiyeretso chimene akapanda ichi, palibe m'modzi adzaonane ndi Ambuye" (Ahebri 12:14). Ndi mphamvu ya Mzimu Woyera timatha kumvera lamuro lakuti, "Mudzikhala woyera mtima, pakuti Ine ndine woyera Mtima" (1 Petro 1:15-16.

Chiyeretso chimaoneka mwa wokhulupilira pamene iye azindikira za kuyanjana kwake ndi Khristu mu imfa yake ndi kuuka kwake, kudziwerengera kwake kwa tsiku ndi tsiku pa choonadi cha umodzi, ndi kudzipereka chiwalo chake chilichonse kuti chilankhuliridwe ndi Mzimu Woyera nthawi zones (Aroma 6:1-11; Aroma 8:1-2, 13; Agalatiya 2:28; Afilipi 2:12-13; 1 Petro 1:5).

**J. Mpingo**

Mpingo ndi Thupi la Khristu mokhalamo Mulungu mwa Mzimu, wokhala ndi udindo wokwaniritsa lamuro lalikuru loperekedwa ndi Ambuye. Wokhulupilira aliyense, wobadwa ndi Mzimu, ali ndi gawo lenileni la Msonkhano wa Onse ndi Mpingo wa Wobadwa Woyamba wolembedwa m'Mwamba (Aefeso 1:22-23; 2:22; Ahebri 12:23).

**K. Utumiki**

Utumiki woitanidwa ndi Mulungu ndi woikidwa kolingana ndi Malembo, unapelekedwa ndi Ambuye wathu ndi cholinga chakufalitsa Uthenga Wabwino ku dziko lonse lapansi, ndi kumangilira thupi la Khristu (Maliko 16:15-20; Aefeso 4:11-13).

**L. Machiritso ndi Mphamvu ya Mulungu**

Machiritso ndi mphamvu ya Mulungu ndi gawo lenileni la Uthenga Wabwino. Kulandiritsidwa ku matenda kumene kupezeka muchiyanjano ndi Ambuye ndi cholowa cha okhulupilira onse (Yesaya 53:4-5; Mateyu 8:16-17: Yakobo 5:14-16)

**M. Chiyembekezo Chodala**

Kuuka kwa iwo amene anamwalira ali mwa Khristu ndi kukwatulidwa kwao pamodzi ndi iwo amoyo otsalira pa nthawi yakufikanso kwa Ambuye ndiko chiyembekezo chimene chayandikira komanso chodala cha Mpingo (Atesalonika 4:16-17; Aroma 8:23; Tito 2:13; 1 Akorinto 15:51-52).

**N. Ufumu wa Khristu wa Zaka Chikwi**

Mu kubweranso kwachiwiri kwa Khristu muli kukwatulidwa kwa oyera mtima, chimene ndi chiyembekezo chathu chodala, kotsatizana ndi kubweranso kooneka kwa Khristu pamodzi ndi oyera mtima ake kudzalamulira pa dziko lapansi zaka chikwi chimodzi (Zakaliya 14:5; Mateyu 24:27, 30; Chibvumbulutso 1:7; 19:11-14; 20:1-6). Ulamuliro wa zaka chikwi udzabweretsa chipulumutso cha fuko la Israeli (Ezekiel 37:21-22; Zefania 3:19-20; Aroma 11:26-27) ndi kukhazikitsidwa kwa mtendere pa dziko lonse lapansi (Yesaya 11:6-9; Masalimo 72:3-8; Mika 4:3-4).

**O. Chiweruzo Chotsiriza**

Padzakhala chiweruzo chotsiriza pamene akufa ali mu uchimo adzaukitsidwa ndi kuweruzidwa kolingana ndi ntchito zawo. Yense amene sadzapezeka wolembedwa mu buku la moyo, pamodzi ndi mdyierekezi ndi amithenga ake, chirimbo chosokeretsa ndi m'mneneri wonyenga adzaponyedwa ku chilango chosatha, m'nyanja ya moto ndi sulfure, imene ili imfa yachiwiri (Mateyu 24:46; Maliko 9:43-48; Chibvumbulutso 19:20; 20:11-15; 21:8)

**P. Mwamba mwatsopano ndi Dziko latsopano**

"Koma monga mwa lonjezano lake, tiyembekeza mwamba mwatsopano, ndi dziko latsopano m'menemo mukhalitsa chilungamo" (2 Petro 3:13; Chibvumbulutso 21:22).